


NKHOSA YOTAYIKA

*Phunziro la Fanizo la Yesu Kuchokera pa
Luka 15:3-7*



WOLEMBA

F. Wayne Mac Leod

LIGHT TO MY PATH BOOK DISTRIBUTION

Sydney Mines, Nova Scotia, CANADA

WOTANTHAUZIRA MCHICHEWA

Brother Francis Ananda Chipukunya

Going Home Africa Ministries

P.O.Box 280, Liwonde, Malawi

Cell: +265 888 774 463

EMAIL: mchikkwawa@yahoo.com

Nkhosa Yotayika

Kulembedwanso Mchingerezi mwezi wa August 2015

Kutanthauzidwa mchichewa koyamba mwenzi wa February 2022

Copyright © 2022 by F. Wayne Mac Leod

Chilolezo ndi cha eni ake a bukuli. Buku lino lisagwiritsidwe ntchito mwa njira ina iliyonse popanda chilolezo cha eni ake omwe ndi a Light To My Path Book Distribution.

Pokhapokha ngati zaonetsedwa, Mawu onse a Mulungu m' buku lino anatengedwa m' Buku Lopatulika la New International Version la chaka cha 1973, 1978, 1984, lolembedwa ndi International Bible Society malingana ndi chilolezo chochokera ku Zondervan Publishing House. Malamulo onse anatsatidwa.

Ulemu wapadera upite kwa amene adawerenga bukuli kuti lifike pano, chifukwa popanda iwo, izi sizidakatheka.

Diane Mac Leod, Lillian Mac Neil

Zamkatimu

CHIAMBI.....	5
1 - UDINDO WA M'BUSA.....	9
2 - NKHOSA YOTAYIKA	15
3 - Kukhala mu Nkhosa 99	27
4 - Kupita Kofunafuna Nkhosa Yosochera	33
5 - Ndipo Pamene Adayipeza Iyo	41
6 - Sangalalani Nane Pamodzi.....	51
7 - Kusangalala Kumwamba.....	59
Light To My Path Book Distribution.....	69

CHİYAMBI

Ili ndi phunzira la Luka 15:3-7. Pamene nkhani iyi imagwiritsidwa ntchito pa cholinga chosodza anthu, koma ine cholinga changa ndikuonetsa mmene nkhanayi ingapindulira munthu okhulupirira.

Fanizo lino tsopano likudziwika kuti “Fanizo la nkhoa yotayika.” Mawu oti “tayika” ndi mawu a Fiyoloje amene akugwiritsa ntchito kwambiri masiku ano. Monga mawu a Fiyoloje, iwo akuyimira munthu wosakhulupirira amene asanalandire chipulumutso cha Ambuye athu Yesu Khristu. Timanena kuti munthu ndi wotayika chifukwa asanalandire Yesu Khristu. Koma ine sindikugwiritsa ntchito mawu oti “Tayika” mwanjira imeneyi.

Ine ndakumana ndi okhulupirira ambiri amene athedwa nzeru pa chikondi ndi kudzipereka komwe analinako kale. Koma kwa ena moyo udali wowawa ndipo chikhulupiro chawo chidaonongeka pamapeto pake. Kwa ena, mpingo sunkawakonda, ndipo adapezeka akungoyendayenda kunja kwa chiyanjano cha okhulupirira. Ena adagwa mmayesero adzikoli ndipo kudzipereka kwawo kwa Yesu kunatha. Okhulupirira awa ataya njira yawo. Achoka panjira imene Mulungu anawakonzera. Iwo ndi nkhoa zotayika tsopano.

Ngakhale Yesu amene ndi m’busa wabwino ankadziwa kuti nkhoa zake zidzavutika pa dziko lapansi. Pali adani ambiri a nkhoa pa dziko lapansi. Chikhulupiro cha izo chikuyesedwa kwambiri. Nkhosa zina za Ambuye zathamangangitsiridwira kutali. Zina

zavulazidwa ndipo zili ndi mabala, ndipo zatayidwa pambali pa njira yopita ku moyo wosatha.

Lino ndi fanizo lofotokoza kubwezeretsedwa kwa nkhoa zotayika zomwe zataya njira zawo ndi kuthawa pa chimwemwe ndi chiyanjano chimene Mulungu anakozera izo. Izi zikupatsa ife ntchito, kuti tikathandize abale ndi alongo amene chikhulupiriro chawo chosweka ndipo chili ndi mabala. Pamene Yesu adaphunzitsa phunziro lino, Afarisi ndi atsogoleri a chipembedzo adaleka kusamalira anthu amene adali pansi pa ulamuliro wawo. Nkhosa sizimaphunzitsidwa. Padalibe woti mkuzisamalira. Zinkangoyendayenda kuchoka pa choonadi ndikumakagwa mnjira za dziko pamene azibusa awo angokhale chete pambali pa izo ndi kuzisiya ziziwonongeka.

Mnjira zambiri fanizo lino likufotokoza kuti tiyenera kukhala abusa a nkhoa za Mulungu okhulupirika. Likuvumbulutsa chikhumbo cha Ambuye Yesu kwa anthu ake ofunikira amene ataya njira yake. Uku ndi kuyitana kwa onse amene angamve chiphunzitsochi kuti amve cholinga cha Mulungu kwa amene chiyanjano ndi chimwemwe chawo mwa Yesu Khristu cha zimitsidwa. Utumiki uwu siwophweka ayi. Koma ndi umene umasangalatsa mtima wa Mulungu. Ndikukhululupirira kuti madalitso ambiri a Mulungu agona pa onse amene amatumikira nkhoa zotayika kuti zibwerere kwa Mulungu.

Lino sibuku loti kodi tipange zinthu motani. Ndalisiya buku lino mmanja mwa azibusa oyenerera. Cholinga changa ndikufotokozera fanizoli ndi kuvumbulutsa cholinga cha Mulungu ku mpingo wa lero lino. Ndi pemphero langa kuti buku lino livumbulutse cholinga cha Mulungu mwatsopano ndi mwachilendo. Tiyeni timulole Mulungu kuti agwiritse ntchito

bukhu lino kuti nkhusa zake zotayika zibwerere kwa lye ndipo kuti zikadziwe kukoma mtima kwake.

F. Wayne MacLeod

1 - UDINDO WA M'BUSA

*Ndipo Yesu anawafotokozera fanizo lino:
Tangoganizani mmodzi wa inu ali ndi
nkhosa zana limodzi -100(Luke 15:3-4)*

Pa Luka 15:3-7, Baibulo silingonena za nkhosa yotayika chabe mmene imakhalira ikasokera ndi zimene zimachitika kuti ipezeke. Koma apa Yesu akunena za atogoleri a chipembedzo alero lino. Atsogoleri awa adamunyoza Yesu chifukwa chodya ndi ochimwa ndi otolera mitsonkho. Kwa iwo, mtsogoleri wa chipembedzo adalibe ufulu wodzidetsa kudzera mnjira yodya ndi ochimwa ndi okhometsa msonkho. Koma Yesu adayankha mitsutso yawo kudzera powafotokozera fanizo.

Fanizo lino limagwiritsidwa ntchito polimbikitsa akhrisitu kuti akalalikire anthu osakhulupirira. Palibe funso apa loti kodi veseri likutero. Koma tsopano tatiyeni tiwonepo fundo zina apa mwatchutchu.

Tiyeni tiwone kuti nkhosa zomwe Yesu akunena pano zidali panso pa ulamuliro wa m'busa. Kuyankhula kwa atsogoleri achipembedzo nthawi yakeyo Yesu adati "Tangoganizani munthu ali ndi nkhosa zana" (vesi 4). Izi zikutanthauza kuti nkhosa imene akunena idali pakati pa zizake ndiponso panso pa ulamuliro wa mtsogoleri wa Uzimu.

Chachiwiri, taganizani za zimene Yesu adanena zokhudza nkhosa pa Mateyu 25:31-33:

Nkhosa Yotayika

Pamene Mwana wa munthu adzabwera ndi ulemmero wake, ndi angelo ake, lye adzakhala pa mpando wake wa ulemmero wa chifumu Kumwamba. Mayiko onse adzanza kwa lye, ndipo lye adzasiyanitsa anthu monga momwe m'busa amasiyanitsira nkhoa kwa mbuzi. lye adzayika nkhoa kudzanja lake la manja ndipo mbuzi kudzanja lake la mazere.

Wonani kusiyana apa kwa pakati pa mbuzi ndi nkhoa. Nkhosa ndi zomwe zili za m'busa wabwino amene ndi Ambuye athu Yesu Khrisitu. Mbuzi ndi anthu osakhulupirira amene adamukana Yesu. Izi zikutanthauza kuti nkhoa zimene Yesu amanena apa si anthu osakhulupirira kwemi-kweni. Apa zikuonetsa kuti ankanena za okhulupirira amene ali pansi pa chisamaliro cha m'busa wauzimu. Awa ndi amene apambuka panjira yawo ya choonadi. Ndi zoona kuti ochimwa amene Yesu adanyozedwera chifukwa chodya nawo pamodzi adali pansi pa utsogoleri wina wake, koma ankathawidwa ndi kukanidwa chifukwa cha moyo wawo.

Yesu adayamba fanizoli ndi mawu awa: “Tangoganizani wina ali ndi nkhoa zana” lye akutikumbutsa za atsogoleri a nthawi yake amene adapatsidwa ntchito yosamalira kagulu kena ka anthu owerengeka. Nkhosa zana izi udali udindo wawo. Monga azibusa, adali ndi ntchito yosamalira izo. Uwu udali udindo woti sangautenge kukhala wopanda pake. Werengani zimene Mulungu adanena kwa azibusa ake pa Ezikiel 34:2-6:

“Mwana wa munthu adalosea zokhudza azibusa aku Israel. lye adalosea zaiwo motere: “Ichi ndi chimene Mulungu wa mphamvu zonse wanena: Tsoka kwa azibusa a Israel chifukwa asankha kudzisamalira iwo eni oka! .Kodi m'busa

Udindo wa M'busa

*satenga chisamaliro cha nkhusa zake?
Mukudya mkaka, mukuvala zovala zaubeya
ndi kumapha nyama za ku mtima kwanu,
koma mwasiya kusamalira gulu la nkhusa
zanu. Inu simudazilimbitse zimene zafoka,
kapena kuchiza zimene zikudwala kapena
zomwe zavulazidwa. Simunazibweze
zimene zasochera, kapena kukaziyang'ana
izo. Inu mwazilamulira mwa nkhusa ndi
moipa mtima. Choncho izo zamwazikana
chifukwa ziribe m'busa, ndipo izo
zawwazikana ndikusanduka chakudya cha
nyama za kuthengo. Nkhusa zanga
zikungoyendayenda kumapiri ndi kuzitunda
zitalizitali. Zamwazikana pa dziko lonse
lapansi, ndipo palibe ndi mmodzi yemwe
amene akupita kukazisaka kapena
kukazifunafuna*

Mulungu akudzudzula azibusu a nthawi ya Ezekiel, chifukwa adatenga kukhala oweta nkhusa ndicholinga chofuna kusangalatsa miyoyo yawo. Azibusu awa sakupezera nkhusa zawo zakudya. Chifukwa nkhusazi sizikulandira chisamaliro choyenera, izo zasweka mitima ndipo zamwazikana. Dziwani kuti Ezekiel 34:6 akunena kuti, ngakhale nkhusazi zamwazikana modetsa nkhusa kuchokera kwa azibusu awo, komatu palibe ndi mmodzi yemwe amene akukazisaka kapena kukazifuna izo.

Pamene Mulungu adatiyitana ife kuti tikhale azibusu, Iye adatiyitana ku utumiki ofunikira kwambiri. Uwu siutumiki waphweka. Kusamalira nkhusa ndi utumiki wapamwamba kwambiri. Mulungu adzatifunsa zokhudza nkhusa ina ili yonse yomwe adatipatsa kuti tiyisamalire. Choncho, mveterani chimene Yesu adanena zokhudza amene adzapangitsa nkhusa zake kumwazikana pa Maliko 9:32:

Nkhosa Yotayika

*Ndipo mmodzi mwa inu amene
adzapangitsa mmodzi amene
amakhulupirira Ine kuchimwa, ziri bwino
kwa iye kuponyedwa mnyanja yozama
atamangiridwa chimwala pa khosi pake.*

Mulungu amayembekezera azibusa kuti azichenjeza ndi kutetezera nkhusa zake pamene ziri pa ngozi. Iye adanena ichi momveka bwino kwa Ezekiel kuti, ngati sadzachenjeza nkhusa zimene ziri pansu pa chisamaliro chawo ku zoopsa, mwazi wa izo udzakhala pa manja awo. Iwo adzayankha mulandu pachimene chidzagwere nkhusa imene amayenera kuyichenjeza. Tiwerengani Ezekiel 3:18 pamene kunena kuti:

*Pamene ndinena ndi munthu wachimwa,
kuti zoonadi iwe udzafa, ndipo iwe
sudamuchenjeze kapena kumuyankhula
kuti asiye njira zake zoipa kuti apulumutse
moyo wake, munthu woipa ameneyu
adzafa chifukwa cha tchimo lake, ndipo Ine
ndidzawerengera mwazi wake pa iwe.*

Azitsogoleri a nthawi ya Yesu sankagwira ntchito yawo. Anthu a Mulungu ankangoyendayenda ndi kumagwa mmachimo osiyanasiyana. Iwowa ankangopanga zofuna zawo ndi zosangalatsa iwo eni ndi kuyiwala kusamalira nkhusa zimene ndidawapatsa. Izi zikutiuza kuti Afarisi ndi azitsogoleri ena ankathawa atolera misonkho ndi wochimwa, ndi kumanena kuti ndi chinthu chonyasa kumaphatikirana ndi anthu amenewa.

Pamene Yesu akunena pano za m'busa yemwe adali ndi nkhusa zana limodzi, Iye akunena za mtsogoleri amene adamupatsa ntchito yayikulu ya Mulungu yosamalira, kutumikira ndi kupezera zosowa nkhusa zimene ziri pansu pa ubusa wake. Mwachidule tonse ndife azitumiki. Mulungu waika azibambo, azimayi,

Udindo wa M'busa

anyamata ndi atsikana munjira zathu ndi kutiyitana kuti tikasamalire nkhoa zake.

Fanizo lino sila azibusa a Uzimu okha , koma ndi la wina aliyense amene wapatsidwa mphamvu ndi udindo pa mzake. Mundine zotsatirazi, ife tidzaona mmene Ambuye athu Yesu Khrisitu akutiphunzitsira zokhudza mtima wake ndi udindo wathu pa abale ndi alongo amene akungoyendayenda ndi dziko ndipo asokera njira zawo.

Zoyenera Kuziganizira mwapadera:

- Kodi azibusa ndi ndani mufanizoli? Nanga kodi apatsidwa ntchito yotani?
- Kodi tizingoona nkhoa pano ngati anthu osakhulupirira amene sadamvomereze Yesu, kapena fanizoli likukhudza wina aliyense amene wataya njira yake? Fotokozani
- Taganizirani dera lomwe mukukhala. Kodi kuli okhulupirira amene anataya njira zawo ndi kuthawa pachiyanjano ndi Mulungu? Kodi mpingo wanu ukuchitapo chiyani pazokhudza anthu amene achoka pa choonadi, kapena akhumudutsidwa pa njira yawo ya Uzimu?
- Kodi Mulungu adatipatsa ife udindo pa munthu wina? Kodi ndi anthu ati amene Mulungu watipatsa kuti tiwasamalire? Kodi takhala wokhulupirika kumayitanidwe athu?

Zofunika Kuzipempherera:

- Kodi mukudziwa munthu wina amene wachoka pa choonadi kapena wakhumudutsidwa pa moyo wake wa Uzimu? Tengani kanthawi ndi kumupemphera.

Nkhosa Yotayika

- Mpempheni Mulungu kuti akuonetseni anthu amene wawaika kuti muwasamalire. Mpempheni Mulungu kuti mukhale wokhulupirika pamene mukusamalire amene wakupatsani. Mpempheni Mulungu kuti akuonetsereni chimene muyenera kuchita pamene mukutumikira nkhoa zake pa nthawi ya zosowa za izo
- Tengani nthawi ndi kupempherera azibusa apa mpingo wanu. Mpempheni Mulungu kuti atipatse chisomo chake kuti zikamve mawu ake ndi ku wasunga.

2 - NKHOSA YOTAYIKA

*“Tangoganizani munali ndi nkhusa zana
limodzi ndipo mwataya imodzi. (Luka 15:4)*

Nkhosa zosathandinza pachirengedwe. Ziribe mphamvu zachirengedwe zodzitetezera zimafuna wina azisamalire. Pamene Yesu anaona chigulu cha anthu chikumulondala tsiku limodzi, anafanizira ndi nkhusa zosathandizazi zikusowa m’busa. Mtima wake unadzazidwa ndi chisoni ndipo anauza ophunzira ake kuti alirire Ambuye mwini zokolola kuti atumize antchito kuti awasamalire:

*Ataona maguluwo, anagwidwa ndi chisoni
chifukwa anali ozunzika ndi osowa
chithandizo ngati nkhusa zopanda m’busa.
Pamenepo anati kwa ophunzira ake,
‘zokolola ndi zambiri koma antchito ndi
ochepa. N’chifukwa chake, pemphani
Ambuye mwini zokolola kuti atumize
antchito ku munda wake’. (Mateyu 9:36-38)*

Nkhosa imakhala ndi adani ambiri. Nkhosa ya uzimu imayenera ikozekere mayesero ndi kuyesedwe, zomwe zimapanga nkhanza zomwe zimapangitse kuti zibalalike. Tiyeni titenge kanthawi tiganizire za njira zina zomwe okhulupirira angathe kukhala munjira yomwe Mulungu wawakozera.

Mavuto a Fiyoloje

Choyambirira, nkhosa zingathe kusokokera kamba ka chiphunzitso cha fiyoloje. Chomwe chingapangitse mawu a Mulungu kuti akhale olakwika. Mulungu anatsutsa za mipingo yosakhulupirira Iye pokhala nyambo paziphunzitso zolakwika za Nikolai zomwe zikupezeka mu Chivumbulutso 2:15-16:

Chimodzimodzinso inuyo muli ndi ena amene amatsatira ziphunzitso za Anikolai. Tsono tembenukani mtima. Mukapanda kutero, ndidzabwera kwanuko posachedwa ndipo ndidzachita nanu nkhondo ndilulunga lotuluka m'kamwa mwanga lija

Zolembedwa pa Agalatiya 3:1-3 Mtumwi Paulo anakamba zaokhulupirira pokhala iwo aphunzitsi onyenga amene amalimbikitsa kusamala malaumlo a Mose ngati njira yokapulumukira. Polemba ku Agalatiya Paulo anati:

Agalatiya opusa inu, anakulodzani ndani? Timaonetsa poyera pamaso panu Yesu Khristu munga wopachikidwa pa mtanda. Ine ndikufuna ndiphunzire kuchokera kwa inu chinthu chimodzi ichi: Kodi munalandira Mzimu pochita ntchito za lamulo, kapena pokhulupirira zomwe munamva? Kani ndinu opusa chotere? Inu mutayamba ndi Mzimu, kodi mukufuna kutsiriza ndi ntchito za nthupi?

Afarisi anali atsogoleri opatsidwa ulemu munthawi imeneyo. Pamene, poyankhula kwa iwo mu Mateyu 23:15 Yesu anati:

Tsoka kwa inu, aphunzitsi amalamulo ndi Afarisi, achiphamaso! Mumayenda

Nkhosa Yotayika

*maulendo ambiri pamtunda ndi panyanja
kuti mutembenuze munthu modzi, ndipo
akatembenuka, mumasandutsa kukhala
mwana wa gahena kawiri kuposa inu.*

Kutengera ndi chiphunzitso cha Yesu, Afarisi amenewa anali achiphamaso amene amasintha anthu kukhala **“Ana a gahena.”** Ngati m’busa wabwino, Yesu anawachenjeza ophunzira ake paziphunzitso za Afarisi ndi aphunzitsi amalamulo pa Mateyu 16:5-12. Samafuna kuti ophunzira ake agwe nawo munyambo zawo.

Pali ziphunzitso zonama zambiri masiku ano. Ngakhale okhulupirira enieni amatha kunamizidwa ndikugwa mumalemba awo wonama. Adani achiphunzitso cha fiyolojewa angathe kupangitsa kuti nkhusa isokere kwa zaka mumnjira yomwe ili yolekana ndi Mulungu ndi zolinga zake pa miyoyo yawo. M’busa wabwinoyi amayenera adziwe za adani amenewa achiphunzitso cha fiyoloje amene amabwera kuti awononge nkhusa ndipo apange chilichonse chomwe angathe kuti ateteze kumavuto amenewa.

Tchimo

Ana a Mulungu sikuti angathe kusochera ndi ziphunzitso zokha za fiyoloje ayi, komanso angathe kugwa muuchimo. Paulo anawakalipira Akorinto chifukwa sanachitepo kanthu pa mwana amene anagona ndi mkazi wa bambo wake (onani 1 Akorinto 5:1). Pa 2 Timoteyo 4:10 pali zolembedwa za mzibambo wina dzina lake Dema amene Paulo anamusiya chifukwa cha chikondi chake kuzinthu za dzikoli. Pali mayesero osawerengeka kwa munthu okhulupirira. Nkhosa sizinakozekere mayesero amenewa. Onetsetsani mwachangu pa mpingo wanu. Pali umboni wa

Nkhosa Yotayika

okhulupirira akugwa muuchimo? Mdani wathu Satana ndiwochenjera. Dziko ili ndi njira zake zimaoneka zokopa ndipo nkhusa zambiri zimachotsedwa kuchoonadi kumapita kuuchimo ndi kuzoyipa.

Nkhosa yakugwa nthawi zina imakankhidwa kumbali ndi nkhusa zina zomwe sizifuna kuti zikhudzidwe nawo ndi iwo. Nthawi zina amachita manyazi ndikulephera kwawo ndipo mpaka samva kuti abwerere ku zizawo. Ngati nkhusa yosochera imayenda opanda oyitsogolera, osadziwa kuti Mulungu awakhululukira kapena azawo akwamvomera.

Kukondana ndi Mulungu

Nkhosayo ingathenso kusochera mumchikondi cha Mulungu. Mpingo waku Aefeso ndi chitsanzo chabwino. Mvetserani kuzotsatira za Ambuye kumpingo umenewu pa Chimvumbulutso 2:4-5:

“Komabe ndili chotsutsana nawe: Wataya chikondi chako chapoyamba. Kumbukirani kuti munagwa kuchokera patali. Lapa ndikuchita zinthu zimene unkachita poyamba, ngati sulapa ndidzabwera ndikukuchotsera choyikapo nyali chako pamalo ake.”

Mpingo waku Aefeso unali wamphamvu mumawu ndi ulemerero, koma atsogoleri ake amataya chikondi chawo chapa Yesu. Ambuye anawachenjeza kuti akufunikira alape ngati salapa adzawachotsera choyikapo nyali chawo pa malo ake. Kodi ndizosamvuta motani kuti mugwidwe muchitetezo cha chilungamo kapena mukukuziriza umfumu wa Mulungu?. Izi sizoyipa pazokha koma ngati zimatenga

Nkhosa Yotayika

malo athu a ubale wathu ndi Mulungu, timakhala oyipa ndi adama. Tingathe kupembedza choonadi koma osati opatsa choonadiyo. Tingathe kukonda mmene mzindawo uliri ndi zinthu zake koma osati kukonda mfumu ya mzindawo

Nthawi zina anthu a mumpingo amataya chikondi chawo chopoyamba, kuikapo zinthu zina mmalo mwake monga , zomangamanga, zochitika, zikhalidwe ndi zolembe zake. Nkhosa za mipingo imeneyi zimatayika kutali ndi kuzolinga za Mulungu. Kukhala otanganidwa kwawo ndikutetzenza choonadi kwawo zinawachotsa kwa Khristu. Anataya kukwaniritsa kwawo posangalala ndi kuyeretsedwa mwa Mulungu ndi kuyikamo zithu zina, choonadi ndi chikhalidwe. Masalimo anaona izi mwa anthu mu tsiku lake limodzi pamene analira kwa Mulungu pa Masalimo 85:6 :

*Kodi simudzatitsitsimutsanso, kuti anthu
anu asangalale mwa inu?*

Kusowa kwa chikondi chopoyamba kapena kukwaniritsa kusangalala mwa Mulungu ndi nkhani ya kuti nkhoa zonse za mumpingo ziyenera kuyidziwa. Amene anasowekera kukwaniritsa anasokera ndikupita kuchikhulupiriro chonama chomwe sichingakwanitse mokwanira mzimu wawo. Nkhosa imeneyi ikuyenera ibwezeretsedwe.

Maubale

Palipano nkhoa zina zimasokera chifukwa cha maubale abwino amu mpingo. Paulo anawapempha atsogoleri awiri ampingo waku Afilipi kuti akoze maudani awo pa uwiri wawo. Afilipi 4:2 pankhaniyi anati :

Nkhosa Yotayika

*Ndikudandaulira Yuwodiyayo ndi Sintikayo
kuti akhale ndi mtima umodzi mwa
Ambuye.*

Kodi ndi ndani pakati panthu amene sanalakwiranepo ndi zake mu mpingo? Kodi ndikangati komwe milandu yathuyi inabweretsa kugawikana mu mpingo? Ngakhale okhulupirira akhudzidwa ndi zinthu monga kuweruza milandu mosalondola ndi kudzikonda mu mpingo. Mtumwi Yakobo anachenjeza mpingo pa nkhani ya kudzikonda, kuwakumbutsa kuti izi sizimalimbikitsa kuti kukhale mtendere mu thupi la Khristu. Tiyeni timvetsera Yakobo 2:1-4

*Abale anga, okhulupirira Yesu Khristu
waulemerero, musaonetse tsankho.
Tangoganizirani, pakati panu patabwera
munthu atavala mphete yagolide ndi
zovala zapamwamba, ndipo winanso
wosauka n'kulowa atavala sanza. Ngati
mumasamala kwambiri munthu wovala
bwinoyu uja, n'kumuwuza kuti, “ **Khalani
pa mpando wabwinowu**” koma wosauka
n'kumuza kuti, “ **Ima apo**” khala pansi
pafupi ndi chopondapo mapazi angawa”
Kodi simunachite tsankho pakati panu ndi
kukhala oweruza a maganizo oyipa.*

Taganizirani munthu amene wakanidwa mu mpingo umeneyu wa Yakobo tsiku lalero. Atakhala kuti anabwera kumpingo ndipo munamulandira ngati kuti iye ndiwosafunikira, kusiyana ndi abale ndi achemwali ake, kodi mukuganiza kuti ndi mwatendere motani muthuyi angamve? Angafune kubweranso? Yesu kawirikawiri amapanga maubale ndi anthu amene amakonda kufunsafunsa mafunso. Mpingo wa Chipangano Chatsopano umamvutika ndi kusiyani kwa zikhalidwe. Timawerenga mu Machitidwe 6:1 mmene

Nkhosa Yotayika

a Yuda a chi Hereni amadzionera ndi kudzikonda kwa Ayuda a chiheberi:

M'masiku amenewo pamene chiwerengero cha ophunzira chinkachuluka, Ayuda a Chihelene pakati pawo anadandaula chifukwa cha Ayuda a Chiheberi chifukwa amasiye awo samawagawira chakudya cha tsiku ndi tsiku.

Kusiyana kumeneku kungathe kuonekeranso pamene yesu anapita ku Samaliya, Ndipo anakumana ndi mzimayi pachitsime cha madzi. Timawerenga izi pa Yohane 4:9 kuti Ayuda samagwirizana ndi Asamaliya. Udani wawo unali uja wakuti sakanatha kukhala pamodzi. Kodi ndikangati kamene ana a Mulungu anasokera kuzofuna za Mulungu, chifukwa chakusawerunza nkhani molondola ndi kuwawidwa komwe okhulupirira ena ochokera ku mipingo ina, zikhalidwe zina ndi zokonda zina amakumana nako?

Nthawi zina kusiyana pazipembedzo kungathe kukula mpaka kupembedza kuletsedwa. Timawerenga, mwachitsanzo pa Machitidwe 15:37-39 pakusagwirizana pakati pa Paulo ndi Barnaba pa nkhani ya Yohane Maliko.

Barnaba anafuna kutenga Yohane, wotchedwanso Maliko, kuti apite naye. Koma Paulo anaganiza kuti sichinali cha nzeru kumutenga Yohane chifukwa iye anawathawa ku Pamfiliya ndipo sanapitirire nawo pa ntchito. Iwo anatsutsana kwambiri motero kuti anapatukana.

Ndinakumanapo ndi okhulupirira amene anasochera kwa nzaka zambiri kusowa mpingo, chifukwa cha zomwe amaziona mu

Nkhosa Yotayika

mpingo. Samakhala ngati alandiridwa pa anzawo. Nkhosa zimenezi zinasokera mukupembedza chifukwa cha maubale owonongeka. zowawa zomwe nkhosa zina zinapangiridwa ndizazikulu mokuti zimatenga zaka kuti zithe. M'busa wamzeru amakhala tcheru ndi mdani ameneyu ndipo amapanga zonse zomwe angakwanitse kuti abweretse bata ndikubwezeretsa mabala omwe anabwera ndi nkhosa zinazo.

Mayesero ndi kuyesedwa

Njira ina yomwe nkhosa zimataya njira yake ndi mayesero ndi kuyesedwa. Nthawi zina zimaoneka ngati mdani wabwera ndi mphamvu zonse zodzaononga. Kuyesa kwake kumapangitsa kugwedezeke kwa okhulupirira enieni mpaka amataya chikhulupiriro ndi cholinga chawo. Nthawi zina amatha kumadzifusa za chikhulupiriro chawo. Yohane M'batizi anafusa Ambuye Yesu pamene anali mumayesero akulu amoyo wake. pa Luka 7:20 timawerenga kuti mpaka anasochera kudziwa ngati Yesu analidi Mpulumutsi:

Anthuwo atafika kwa Yesu anati, “Yohane m'batizi watituma kwa Inu kuti tidzakufunseni kuti kodi ndinu anayenera kubwerayo, kapena tiyembekezere wina?”

Kuwerenga mwachidule buku la Yobu mu Chipangano Chakale limaonetsa kuti munthu uyu wa Mulungu analitemberera mpaka tsiku lake lobadwa. Werengani muzoonjenzera nzake pa Yobu 3:11-14

Bwanji ine sindinaonongeke pamene ndinkabadwa ndi kufa pamene ndimatuluka m'mimba? Chifukwa chiyani panali

Nkhosa Yotayika

mawondo wondilandirirapo ndi mawere woti andiyamwitsepo? Pakuti tsopano bwenzi ndiri gone mwatendere; ndikakhala nditagona tulo ndi mpumulo pamodzi ndi mafumu ndi aphungu a dziko lapansi, amene anadzamangira nyumba zikuluzikulu zimene tsopano ndi mabwinja

Mneneri Eliya, atayesedwa kwakukulu pa phiri la Carmel, anapeza malo odekha ndi kupemphere kwa Mulungu .Werengani 1 Mafumu 19:3-4:

Eliya ataona zimenezi, ananyamuka nathawa kupulumutsa moyo wake. Atafika ku Beriseba ku Yuda, anasiya mtumiki wake kumeneko, ndipo Eliyayo anayenda ulendo wa tsiku limodzi m'chipululu. Anafika pa kamtengo ka tsache, nakhala pansi pa tsinde lake napemphera kuti afe, "Yehova, ine ndatopa nazo. Chotsani moyo wanga, ineyo sindine opambana makolo anga."

Munthu wamkulu wa Mulunguyi samafuna kukhalanso ndi moyo. Anali atatopa nazo. Atayensa mayesero ake anaona kuti anali akuti sakanatha kuwasenza. Amafuna athawe mayitanidwe ake kwa Mulungu kuti iye afe.

Anthu amenewa anayensa mayesero awo ndikuyesedwa kwawo pa moyo wawo ndipamene anaona kuti kulibwino kuti amfuse Mulungu cholinga chawo chokhalira ndi moyo. Anali ngati nkhusa zosowa ndi zosathandinza okozeka kuti ataye chikhulupiriro. Kodi ndi okhulupirira angati amene ali munyengo ngati zimenezi lero? Kuyesa kwa mdani kwafika pachimake. Asiyidwa ndi mabala ndi

Nkhosa Yotayika

pambalambanda ndi opanda ntchito konse. Atayika, ndi kudabwa kuti ntchito yawo ndi chani mu ufumu wa Mulungu.

Kusalidwa

Chomaliza, mzotheka kuti nkhusa isochere kamba kakusalidwa. Pa Mateyu 9:36-38 Yesu anamva chisoni kwa chigulu cha anthu chifukwa anali ngati nkhusa zopanda m'busa. Kunalali Atsogoleri ampingo ambiri ku Israeri, masiku ameneyo koma samagwira ntchito yawo. Samasamala nkhusa zawo. Afarisi amakana ochimwa, ndipo amakana kukhala nawo pa ubale. Kukana nkhusanzo kukutanthauza kuti ambiri amasochera kuziphunzitsa zonama ndi moyo wauchimo. Abusa amenewa samadyetsera ndi kusamalira nkhusa ndipo ndi chifukwa chake ambiri amatayika ndikugwa mu uchimo.

Tiyenera tidziwe chinthu chimodzi: Mdani wathu sakupuma kuti awononge ntchito za Mulungu. Mphamvu zake zambiri zimayikidwa pa mipingo komaso makamaka kwa nkhusa yopanda zodzitetezera. Sangayime pachilichose mpaka atiyimeza.

Ndikufuna mundimve bwino pano. Sitikukamba sakusowa chipulumutso ayi. Pamene chipulumutso chathu ndichotetezeka, kuyesedwa kwa okhulupirira zimasocheretsa kuziphunzitsa zonama, makhalidwe a uchimo kapena wina kumadziona kuti watayidwa ndi mpingo zoona. Mulungu amakhudwidwa ndi nkhusa izi zosochera. Yesu anayamba nkhusa iyi ndi fanizo: “Tanganizirani mmodzi mwa inu ali ndi nkhusa zana limodzi ndipo imodzi yasowa.” Kodi mmaganizo mwathu tikuwakumbikira okhulupirira omwe ataya njira zawo? Pemphero langa ndi lakuti bukhu lino lisangotsekula maso awo okha, komaso amvetsetse kuti tiyenera titsate ziti kuti tipange utumiki umeneyu ndi zosowa nzake.

Zoyenera kuziganizira kwambiri:

- Kodi okhulupirira angathe kutayika kapena iye kusochera njira yake? Kodi okhulupirira angasochere bwanji munjira yomwe Mulungu anawakonzero? Mperekani zitsanzo zina.
- Kodi munamvako kuti mwasochera munjira yanu? Kodi chinayambitsa ndi chani?
- Kodi ndizotheka kuti tikhale nawo mu utumikira ndi oteteza choonadi pamene tinataya chikondi chanthu chapoyamba?
- Kodi muli okhulupirira mumpingo wanu omwe ataya njira yawo? Kodi Mulungu akufuna inu mupange chani?

Zofunika kuzipepherera:

- Muthokozeni Mulungu chifukwa samatisiya tokha, ngakhale tigwe kapena tisokere munjira yake.
- Mupempheni Mulungu kuti akupatseni chifundo ndi mphamvu kuti muone mavuto ndi mayesero anu. Mufuseni kuti akubweretseni chifupi naye.
- Mupempheni Ambuye kuti akuthandizeni kuti muzikonada ndi kuthandzia amene ali mumpingo wanu omwe ataya njira zawo. Mufuseni kuti akuonetseni kuti mupange chani kuti muwabwezeretse kuti akhale panso pa mapanzi ake.
- Tengani kanthawi kuti muwapempherere azibusa a mpingo wanu. Ndipo mupempheni Mulungu kuti awapatse kukhudzika ndi chisamaliro pa nkhusa zosokera.

Nkhosa Yotayika

- Mupempheni Mulungu kuti akupangeni mukhale ogwirizana ndi adani anu amene amafuna kuononga nkhosa yosochera.

3 - Kukhala mu Nkhosa 99

*“ Kodi iye sangasiye 99 zija kutchire. ..”
(Luka 15:4)*

Kodi chinthu chabwino ndichiti chachirengedwe kwa m’busayu kuti achite pamene nkhusa imodzi yasokera kapena ili muzoopswa? Mvetserani mawu a Yesu mu vesi lachinayi: **“Kodi iye sangasiye 99 zija kutchire?”** Tiyeni titengeko kanyengo kuti timvetsetse zomwe Yesu akufuna atiuze pano.

Taganizirani mawu awa: **“Kodi iye.”** Mawuwa akutiiza kuti ndi chirengedwe ndithu kuti ngati nkhusa imodzi yasowa, m’busa wokhulupirika amasiya zimene amapanga ndikukayang’ana imodzi yosocherayo. Pamene m’busa wataya nkhusa imodzi, imakhala milandu yake. Mtima wam’busa wachilungamo umasweka chifukwa cha imene yasowayo. Moyo wake ndi nthanzi lake limakhala muzoopswa. Amapanga chilichose ndi mphamvu nzake kuyiteteza ndi kuyipulumutsa.

Dziwansonni mawu awaso **“Kusiya 99.”** Mawu awa akutionetsa kuti nthawi zina nkhusa zinzano ziyenera kuyikidwa kumbali kwakanthawi kuti musamalire imodzi imene ikufunika kusamalidwayo. Sitikuyenera kuti tione izi ngati kuti akuthawa 99 zija. Ngati pali china, m’busayu akusamala nthanzi lawo pakuyang’ana imodzi yosowayo.

Tangoganizirani kuti mwadzimenya chala chanu chimodzi ndi nyundo. Kodi thupi lanu lonse limapweteka chifukwa cha chala

Nkhosa Yotayika

chimodzicho? Pa 1 Akorinto 12:21-26 Mtumwi Paulo anatiuza momveka bwino mmene izi ziliri mumpingo:

Diso silingawuze dzanja kuti, “Iwe sindikufuna!” M'malo mwake, ziwalo zathupi zimene zimaoneka ngati zofowoka ndizo zili zofunikira kwambiri, ndipo ziwalo zathupi zimene timaziyesa zopanda ulemu, ndizo timazilemeka kwambiri. Ndipo ziwalo zosaoneka bwino ndizo zimalandira ulemu wapadera, koma ziwalo zowoneka bwino, n'kosafunika kuti tizisamalire mwapadera. Mulungu polumikiza ziwalo zathupi, anapereka ulemu wopambana kwa ziwalo zimene zimafunadi ulemuwo kuti pasakhale kugawikana m'thupi koma kuti ziwalo zonse zisamalirane. Ngati chiwalo chimodzi chiumva kuwawa, ziwalo zonse zimamvanso kuwawa, Ngati chiwalo chimodzi chilandira ulemu, ziwalo zonse zimakodwera nawo.”

Mulungu anayika chiwalo chilichose m'thupi pachifukwa ndipo ngati munthu mmodzi wasokera, mpingo wonse umamvutika. Izi zikutathauza kuti m'busa wachilungamo sachepetsa kufunika kwa chinthu ngakhale ndi nkhoa yotchipa ya pagulu lake. Amapanga chilichonse ndi mphamvu zake kuti abwenzeretse nkhoa yosokerayo kuti mpingo ukhale mmene Mulungu amaufunira utakhalira. Ngati nthupi lingakhale la nthanzi, nthawi yambiri ikuyenera iperekedwe pobwezeretsa nkhoa yosowayo. Nkhosa yosokera sikuyenera ikanidwe kapena osalemekezedwa. Mphamvu zonse zikuyenera ziyikidwe poyibwezeretsa. Mpingo wolimba umakhakika pobwezeretsa ndi kupeza nkhoa imodzi yosokerayo ku malo ake ndi kuntchito yake m'thupi la Yesu Khristu.

Kukhala mu Nkhosa 99

Zingathe kukhala zosamvuta kuti m’busayo akhale maso pa nkhusa 99 za bwinozo. Nkhosa 99 izi ndizosamvuta kugwira nazo ntchito kuposa imodzi yosocherayi. Nkhosa izi 99 zimapanga zomwe zimayenera zizipanga. Kawirikawiri zimalimbikitsidwa kuti zigwire ntchito ndi kukhala zokhulupirika kwa m’busayo. Kwa abusa ena zimaoneka ngati zosalondola kuti asiye 99 zija kuti alondole imene yasokera .Komaso makamaka zimafuna kukhala pazizake. Pamene m’busa wachilungamo, sangaganizireko ndikamodzi komwe kuyisiya nkhusa imodzi manja mwa mdani. Mtima wake umasweka chifukwa cha imodzi yosokerayo. Amapanga chilichose chomwe angakwanitse kuti ayibwezeretse nkhusa yotayika pazizake.

Kusiya nkhusa zinazi 99 sintchito yopepuka. Zimafunika mphamvu zambiri kuti abwezeretse imodzi yosocherayi kuposa kugwira ntchito ndi nkhusa 99 zomwe zili pabwino ndi zodekha. Kutengera mmene anthu a m’dziko amaonera ndi bwino kukhala m’busa wankhusa 99 zokhulupirika kuposa imodzi yosochera ndi yowukira zizake. Pamene abusa ena amakhala osafuna kuti asiye nkhusa zina kuti akayang’ane imodzi yosocherayo.

Tiyenera timvetsetse pano kuti kusiya zinzano 99 sikuti ndi kuzikana ayi kapena kuzisiya izo zosatetezeka ayi. Abusa mu nthawi ya Buku Lopatulika samagwira ntchito okha. Pamene m’busa wokhulupirikayo wachoka kukayan’gana nkhusa yosocherayo, amakhulupirira kuti zinazo zisamalika ndi omuthandinza ntchito amene azizionako m'malo mwake.

Dziwani ichiso kuti m’busayo amasiya nkhusa nzake **“Kutchire”** pamene amapita kokafufuza imodzi yosokerayo. Kusiya nkhusa 99 kutchire sikutathaunza kuti kuzisiya muzoopsa ayi. Pamene kunali zoopsa kutchire zimaperekanso phindu. M’busayo ankaona msanga mdani akubwera kutchireko chifukwa kunalibe chinthu chakuti mdaniyo anakabisalako. Izi zimapatsa m’busayo mwayi.

Nkhosa Yotayika

Phindu lina kutchireko ndilakuti kunali malo ambiri okhalako ndi opezako chakudya. Nkhosazo zimakhala zosamalika kutchireko. Asananyamuke kuti akayang'ane yosocherayo amaonetsetsa kuti zinazo 99 zapatsidwa chakudya chabwino ndi chitetezo chokwanira.

Pamene nkhoa 99 zija zasamalidwa kutchire, tsopano zimapereka mwayi kwa m'busa wabwinoyi kuti apite akayang'ane nkhoa imodzi yosocherayo. M'busayo amasiya zinazo zili pabwino ndikupita kumalo osadziwika kuti akayang'ane inayo. Mu m'chaputala chinachi tiona mavuto amene amkakumana nawo poyang'ana nkhoa yosocherayo.

M'mene tikuonera mawu pa vesi 4, tikuyenera tidzifunse tokha mafunso ofunikira monga awa:

- Kodi timagawana nawo mtima wa m'busa amene amayang'ana imodzi yosochera kapena tikuyika mphamvu zathu zonse kusamala nkhoa 99 zabwinozo?
- Kodi nanga mpingo wanu wachitapo chani kwa amene anasochera ndi kutaya njira yawo?
- Kodi timaona phindu kwa osocherayo mumpingo mwathu?
- Kodi timamvetsa kuti iye akapanda kubwezeretsedwe, mpingo onse uvutika?

Nkhosa iliyonse ndiyofunika ndipo imapindula china chake pokhala pazizakenzo. M'busa wachilungamo amadziwa zimenezi ndipo amapanga zomwe angakwanitse kuti abwezeretse nkhoa yosocherayo kuti zina zonse zikhale bwino. Nkhosa imeneyi ndi udindo wake. Tipemphe Mulungu atipatse mtima wosakasaka nkhoa yosocherayo lero.

Zofunika kuziganizira mwapadera:

- Kodi mpingo wanu wawasamala motani amene anasochera kuchoonadi kapena anagwa mu uchimo?
- Pali okhulupirira mu mdera lanulo omwe asokera? Kodi Ambuye akufuna kuti uwapangire chani?
- Kodi ndi chifukwa chiyani zili zofunika kuti tipeze ndi kubwezeretsa osochera? Kodi ndi zofunikira motani kumpingo wanu kuwabwezeretsa osochera?
- Kodi ndi chifukwa chiyani kusamalira 99 zija ndikwabwino kudzikoli? Kodi ndi mavuto ati amene osaka zosochera amakumana nawo?
- Kodi kuzisiya 99 zija zikutathauza kuti sizofunikira? Kodi ndi phindu lanji ku nkhoa 99 ngati imodzi yawo yabwezeretsedwa?
- Tamuganizireni modzi amene wasokera pa azake. Kodi n'chifukwa chiyani mpingo ungaufune munthu otereyu? Kodi ndi mphatso zANJI zomwe Mulungu amapereka chifukwa cha munthu mmodziyo? Nanga kusowa kwa munthu ameneyu mpingo umasowekeka chani?

Zofunika kupempherera:

- Mufunсени Mulungu atsekule maso anu kunjira zimene okhulupirira mumpingo wanu anasocherera. Mufunсени Ambuye kuti akupatseni mtima wozama othandiza amene akudwala ndi kuzuzika pakati pathu.

Nkhosa Yotayika

- Tenganjani kanthawi kupempherera amene anasochera pa azake. Mufunsi Mulungu kuti awadalitse ndi kuwathandinza kuti abwerere ku mpingo, iye komanso ndi ena.
- Muthokezeni Mulungu kuti nkhoa cholandira nkhoa iliyonse kwa Iye. Ndipo mthokozeni kuti samatoperapo pamene tagwa ndi kusokera m'njira yathu.
- Mfunsi Mulungu akukhululukireni pakusasamala kwa amene anavutika ndi kusochera inu mukuona.

4 - Kupita Kofunafuna Nkhosa Yosochera

“Kodi iye sangasiye 99 zija kutchire ndi kupita kukafuna yotayika mpaka atiyipeza? (Luka 15:4)

Mum'chaputala chomaliza timaona mtima wa m'busa amene nkhusa yake yatayika. Pamene tikupitirira ndi vesi la chinayi, timaona kuti, poona kuti nkhusa imodzi ija ndiyofunikiranso, m'busayu amasiya 99 napita kokafuna ina ija mpaka atayipeza. Pamene tikuwaganizira mawu akuti **“Kupita”**, kuwazukuta amatathauza zinthu zambiri.

Pamene tiri ndi nthawi yowapempherera amene asocherawo, uthengawu ukutiiza kuti pali zinthu zofunika kuti zipangidwe pofuna-funa nkhusa imeneyi. Mtumwi Yakobo amalimbikitsa atsogoleri ake kuti ayike chikhulupiriro pankhani yomwe ikukhudza m'chimwene ndi m'chemwali amene akuoneka kuti akufunikira. Anayankhula kwa omwe amafuna kuti m'bale wawo akakhala bwino amutumize ndikumusiya opanda chithandinzo. Yakobo 2:15-17 anati:

Tangoganizirani m'bale kapena mlongo amene ali ndi usiwa, ndipo alibe chakudya cha tsiku ndi tsiku. Ngati mmodzi wa inu amauza kuti, “Pita ndi mtendere, ukadzifunire ndipo ukakhute,” koma

*Nkhosa Yotayika
osamupatsa zimene akuzisowa, phindu
lake n'chiyani pamenepo?*

Kukhudzika ndi kofunikira kuposa chifundo ndi kuyankhula. Zimafunika kuchitapo kanthu ndi kudzipereka msembe. M'busa sikuti ndiofunika kuti apemphere chabe ndi kukhulupirira kuti chilichonse chitheka. Amayenera adzipereka kuti achitepo kanthu pothandiza nkhoa zosochera. Ndipo iye amayeneranso kukhala okozeka kudzipereke nsembe kuti awone kuti nkhoa yabwezeretsedwa kukhala kwake.

Kupita kokayang'ana nkhoa yosochera zikuonetsa kuti ayenera kukonzekera kuponda matope ndi mavuto ena ambiri. Yesu anatchula kuti amagwirizana ndi ochima ndi okhometsa misonkho. Amadya nawo limodzi ndi kumakhala nawo limodzi. Atsogoreri ampingo a nthawi ya Yesu anali ndi mavuto enieni ndi zimenezi. Pa Maliko 2:16 anthu anafunsa ophunzira ake a Yesu kuti chifukwa chiyani amakhudzidwa ndi ochimwa.

*Pamene aphunzitsi amalamulo ndi Afarisi
anamuona akudya ndi, 'ochimwa' ndi
amisonkho, anafunsa ophunzira ake kuti, “
chifukwa chiyani amadya ndi olandira
msonkho ndi ochimwa?”*

Atsogoleri awa sanali okozeka kuti “**adetsedwe**” pakukhala pamodzi ndi amene anasochera pa chikhulupiro. Chilungamo cha nkhani imeneyi, ngati tikufuna tikawafikire osochera, tikuyenera tipite kumene tingakawapeze. Ngati tikuopa kuti tiziyakhulana ndi “**ochimwa**” kodi nanga tingakumane nawo bwanji? Yesu ankakumana nawo osochera. Amadya nawo ndipo amakhala nawonso limodzi. Koma samakhudzidwa nawo mu uchimo, koma samaopa kuwakhudza kapena kukhala nawo.

Kupita Kofunafuna Nkhosa Yosochera

Mdani wathu sangakondenso china kuposera kuti ife tiziopa dzikoli ndikukana kufuna nkhusa yosochera. Atsongoleri ampingo anthawi ya Yesu anali ndi mantha kuononga mbiri yawo kuti mpaka amaonerera nkhusa yosochera ikuonongeka kusiyana ndi kuyikhudza ndi mawu a Mulungu.

Kodi okhulupirira amaganiza chani akakuona ukupita kunyumba ya osochera kapena amene akukhala mu uchimo? Kodi anagamvetsetse chomwe ukufuna pokumana naye osochera kapena angamve kuti umaonjenzera chikhulupiro chako? Kupita kofuna nkhusa yosochera kukutathauza kuti uzikhudzana ndi ochimwa ndi okhometsa misonkho. Zikutathauza kusiya kufewa ndi chitetengo cha pachigulu ndikuyenda mumisewu ya mumfumbi ndi matope ya dziko lino ndi kuyera kwa Uthenga wabwino. Zikutathauza kukana kugonja. Zikutathauza kuti kusiya mtenedere ndi kuyamba kusamvetsetsetseka. Pali mtengo umene mungalandire pofuna nkhusa yosochera.

Tayankhula zamtengo wa kumvutika kwathu. Tsono, sikuti awa ndi malipiro okhawo. Palinso kuonjezeredwa kwa nthawi, katundu ndi mphamvu. M'busa amene amapita kokafuna nkhusa yake samadziwa kuti zitenga nthawi yochuluka bwanji. Dzaiwani pano, mawu ake popita akuti **“kuyang’ana mpaka atayipenza”**

Amene anatumikirapo kwa wowawidwa ndi osochera amadziwa kuti izi sikuti zimangochitika mwachidule ayi. Nthawi zina zimatenga zaka. Utumiki olimbawu umafunika kulimba mtima ndi kudzipereka kuti nkhusa yovulazidwa ichire ndi kubwezeretsedwa kukhola kwake. Nthawi zina timaona ngati kuti tikupanga zinthu zimene mdani wathu analowererapo kale koma Mulungu amadziwa zimene tikuchita.

Nkhosa Yotayika

Palinso chakuti tiganizire kuti tikamufikire osocherayo. Pali kubwenzeretsana m'mbuyo kwakukulu pa utumiki umenewu. Timadabwa ngati kuti tikwaniritsa. Ntahwi zina zimaoneka kuti mphamvu zanthu zikupita pachabe. Aneneri mu Chipangano Chakale anazona izi mwa Yereimiya amene anthu sankamumvera muthawi yake izi zinaoneka pa Yereimiya 15:15-18:

Ine ndinati, “Inu Yehova, mumandziwa zonse; Kumbukireni ndi kundisasamalira. Ndiripsireni anthu ondizunza. Ndilezereni mtima musandilande moyo wanga. Onani momwe ndi kuvutikira chifukwa cha inu. Munandiyankhula ndipo mawu anu ndinawandira bwino. Mawu anu anandipatsa chimwemwe ndipo mtima wanga unasangalala. Paja ine Yehova Mulungu wamphamvu zonse, ndimadziwika ndi dzina lanu. Sindinakhale nawo gulu la anthu amadyera, sindinasangalale nawo anthu amenewo. Ndinakhala ndekha chifukwa choti dzanja lanu linali pa ine ndipo munadzaza mu mtima mwanga mkwiyo. Nanga n’chifukwa chiyani mavuto anga sakutha? Bwanji chilonda changa sichikupola? Kodi inu munadzakhala ngati m’tsinje wowuma nthawi yachirimwe, Kapena ngati kasupe opanda madzi”

M’busa amene wapiti kofuna nkhusa yosochera amakumana ndi mikwingwirima ya mdani chifukwa safuna kumusiya kuchoka pa chigama pake. Davide anadziwa mavuto amene mbusa amakumana nawo. Kuyankhula kwake kwa mfumu Saulo pa Samueli 17:34-35 anati

Kupita Kofunafuna Nkhosa Yosochera

Koma Davide anati kwa Sauli, “Kapolo wanune ndinkaweta nkhusa za abambo anga. Ndipo mkango kapena chimbalangondo chinabwera ndi kugwira mwana wankhosa pakati pa nkhusanzo, ine ndinatsatira ndi kupha chirombocho. Choncho ndinkapulumutsa mwana wankhosa uja m’kamwa mwake. Ndipo chin’kati chinkandiukira, ine ndinkagwira tchowa lake, n’kuchikantha mpaka kuchipha.

Pamene tapita kofuna nkhusa yosochera nthawi zina tiyenera tikumane ndizokhoma zonse ndi chomwe mdani wachinyamula. Mkango kapena chimbalangondo sizingangosiya chogwira chawo mophweka. M'busayo amayenera ataye moyo wake kuti alande nkhusa m’kamwa mwa mkango kapena chimbalangondo yomwe anayitenga kuchoka pazizake. Amataya moyo kuti apulumutse iyo. Yesu anatiuza pa Yohane 10:14-15 izi ndizomwe anatipangira ife:

Ine ndine m’busa wabwino. Ine ndimadziwa nkhusa zanga ndipo nkhusa zanganzo zimandidziwa. Monga momwe Atate amandidziwa ine, ndiponso ine kuwadziwa atatewo. Ndimapereka moyo wanga chifukwa cha nkhusa.

Kupita kukayang’ana nkhusa yosochera ndi kwa mtengo wapatali. Amene amazitenga izi ngati utumiki amakhala okozeka kutenga zimenzi ndi zolinga zawo, katundu wawo, nthawi yawo ngakhale moyo wawo. Mapemphero awo kwa osocherawo kuti amapanga chilichonse chothekera kuti ayibwezeretse.

- Kodi ili lakhala lokuthandizira m’busa?

Nkhosa Yotayika

- Kodi ili ndilofunikra kwa mpingo wanu, kwa okhulupirira mumaganizo mwanu, kapena kwa amene ataya njira yawo?

Zofunika kuziganizira kwambiri:

- Kodi mudzapeza mphindu lotani mukapita kofuna osochera?
- Kodi kuli mavuto otani popita kofuna nkhoa yosochera?
- Kodi ndi adani otani tikakumane nawo popita kukapulumutsa nkhoa yosochera?
- Kodi zomwe timapanga ngati mpingo zofuna nkhoa yosochera zimabweretsa mphindu lotani kwa iwo?
- Kodi Yesu amayifuna motani nkhoa yosochera imeneyi?
- Kodi tingatani kuti tikuzirize izi?
- Kodi mpingo ukupanga chani polimbikitsa chikondi pa osochera?

Zofunika kuzipempherera:

- Mupempheni Mulungu kuti akupatseni kukhudzika kwakukulu ndi osochera omwe ali maganizo mwanu.
- Muthokozeni Ambuye kuti wakuonetserani chikondi chake pamene munasochera kwa iye.
- Muthokozeni Mulungu kuti wakupatsani chisomo kuti mulimbane naye mdani wanu.

Kupita Kofunafuna Nkhosa Yosochera

- Mupempheni Mulungu kuti akuonetsereni kuti mupanga nawo bwanji osochera omwe wawayika munjira yanu.
- Mupempheni Mulungu kuti akukhululukireni chifukwa chosowa chifundo kwa otayika ndi osowa omwe mwakumana nawo.

5 - Ndipo Pamene Adayipeza Iyo

Ndipo iye atayipeza, anayinyamula paphewa pake mwachimwemwe (Luka 15:5)

Taonani pa vesi 5 chimene m’busa adachita kwa nkhusa yake itapezeka. Pa ndime zino ndifuna nditambasule kapanda mneni uyu **“Ndi chimwemwe adayika nkhusayo pa phewa lake”**

Pamene anapeza nkhusa yotayika ija, m’busa ameneyo akanatha kuchita zinthu zambiri. Iye akantha kukwiya chifukwa nkhusayi yamuzuka kuti ayipeze. Kodi kudali mophweka motani kuti chochita choyamba cha m’busayu kunakakhala kuyipatsa chilango nkhusayi ?. Koma iye sanatero ayi.

M’busayu akanatha

- kuyipidwa ndi kuyidandaula nkhusayi.
- Iye akanayipezera zofooka ndi zolakwitsa nkhusayi.
- Iye akanatha kuyisandutsa nkhusayi kukhala yopanda Uzimu, yosakhulupirika ndi yaupandu.

Zoonadi zinthu izi zikanatha kukhala zoonadi, koma ichi sichinali chimene m’busayu adachita atayipeza nkhusayi.

Taonani chimene m’busayu adachita mfanizoli. Yesu akutiya kuti pamene iye adapeza nkhusayi, mwachimwemwe adayika pa

Nkhosa Yotayika

phewa pake. Chochita chake choyamba chinali cha chimwemwe. Kodi chimwemwe cha m’busachi chikutiiza chiyani zokhudza chikhalidwe chake? Izi zikutiiza kuti cholinga chake sichidali kufuna kuonetsa kuti wavutika, kapena kufuna kuonetsa kukhala wa zauzimu kwambiri. Pamene zinthu izi zili zofunika kwambiri, chokhumba kwambiri cha m’busayu chidali pa nkhusa yake. Pakhala nthawi ina imene tione zifukwa zimene nkhusayi inabalalikira. Koma pano chidwi chathu chikhale pa nkhusa imene yapezeka.

Dziwani chinachake. M’busa anatenga nkhusayo ndikuyiika pa phewa lake. Pali zambiri zomwe tikuyenera tione pano. Dziwani ichi poyamba, m’busayu sakuopa kugwira nkhusa yosochera. Ngati mmene tanenera mobwerezabwereza, izi sizimene atsogoleri ampingo anthawi ya Yesu akanapanga ayi. Amakana kukhala pamodzi ndi ochimwa. Sakanawakhudza kapena kupezeka pomwe pali iwo. Timaona bwino-bwino pa Luka 7:36-39 pamene zimayi **“ochimwa”** anadzodza mapazi a Yesu. Tiyeni tione zomwe anachita Afarisi ataona zimayi uyu akugwira mapanzi a Yesu:

Tsopano mmodzi mwa Afarisi anayitana Yesu kuti akadye naye ku nyumba kwake ndipo anapita nakakhala patebulo. Mayi amene amakhala moyo wauchimo mu mzindawo atadziwa kuti Yesu akudya ku nyumba ya Mfarisiyo, anabweretsa botolo la mafuta onunkhira a alabasta. Iye anayimirira kumbuyo kwa Yesu pa mapazi akulira, nayamba kumadonthenza misozi pa mapazi ake. Ndipo anapukuta mapaziwo ndi tsitsi lake, nawapsopsona ndi kuwathira mafuta onukhirawo. Mfarisiyo anamuyitanayo ataona izi, anati mu mtima mwake, “Ngati akanakhala mneneri,

*Ndipo Pamene Adayipeza Lyo
akanadziwa kuti akumukhudzayo ndi mawu
otani, kuti ndi ochimwa”*

Yesu sanali kuopa kuti akhale pamodzi ndi ochimwa. M’busayu mundime imeneyi akutenga nkhusa yake ndikuyika paphewa kuti ayinyamule bwino. Anayidziwa zosowa zake ndipo anafika kuti ayiphunzitse. Sali ndi nkhusa kuti apezze matope, kapena kuti ena aganize chani akamuona atanyamula nkhusa yosocherayo.

Pamene tikuganizira, mfunso lomwe limabwera m’maganziro: Kodi nanga n’chifukwa chiyani m’busayu akuyenera kuti ayike nkhusayo pa phewa? Pali zifukwa zambiri zopangira zimenezi

Choyamba, nkhusayo yafooka ndipo iribe mphamvu zoyendera payokha. Chikhulupiriro cha osocherayo chakhudzidwa. Mdani watenga malingaliro ake ndi mzimu wake. Nkhusayi ili m’mphetepe mwasewu yobalalika ndi yopanda chochita, yosadziwa kuti ipange chani kapena kuti ibwerere motani kuchipembedzo/kukhola kwake.

Chachiwiri, nkhusa yosocherayo mwina yapuwala miyendo ndipo iri ndi mantha ndi yobalalika. Mwina sakudziwa kuti nkhusa zina zikanena kuti chani zikakayiona iyo ikubwerera. Kodi akumuganizira chani pakuti iye wasokera? Kodi akamulandiranso? Kapena akamusamala mosiyana? Nthawi zina kubalalika ndi manyazi ndi zazikulu kuti abwere.

Chachitatu, nkhusayo mwina yamvulazidwa kwakukulu, kuti kubwerera kukhala kopweteka kwambiri. Mwina sinakozeke kuti ikakhale pamodzi ndi zizake. Izi zimakhala zoonadi makamakaa zikakhala kuti chomwe chapangitsa kuti nkhusayo imvulazidwe ndi nkhusa ina yomwe ndi imodzi mwa abale ndi alongo. Ngati ndi chifukwa chimenechi kuti nkhusayo ikufunika chithadinzo

Nkhosa Yotayika

chapadera kuti m'busayo ayisamale mpaka itachira mpaka kukhala bwino kuti ibwerere.

Pakuyika nkhosayo pa phewa, m'busayo akuonetsa chisamaliro ndi kukhudzika. Ndinkhani ya chikondi ndi chifundo pokhudza nkhoa yomwe yatayika. M'busayo amabweretsa nkhosayo pafupi kwambiri ndi kuyitengera kumalo ena abwino m'banja lake. Ngati nkhosayo anali mwana wachichepere, m'busayo anayikumbatira manja mwake. Koma ngati anali m'chimwene tikanamuthandinza kumuyika manja nkhozi ndi kumutandinza njira yake yobwerera. Munjira ina iliyonse izi mzopangira kukoma mtima , chikondi ndi kuthandinza kwanu.

Kodi ndime imeneyi ikufuna itiuze chani zaudindo wathu ngati okhulupirira kwa amene wasokera munjira yake? Kodi tingamuthandinze ndi kumulimbikitsa motani mlongo wathu? Ndiloleni ndifotokoze njira zina pano.

Kusamalira Osochera

Pamene m'busayo wanyamula nkhoa ndikuyika pa phewa lake, akumulimbikitsa ndi kumuonetsa kulandiridwa kwake ndi chithandinzo. Munjira yomweyo, tikuyenera tikonze malo kuti akhale achirimbikitso ndi a ubale kuti ngati nkhoa ibwerera izidzamva kuti ili mbali imodzi ya zinzake. Anthu ambiri amafuna kubwerera kwa Ambuye ndi ku mpingo koma amaopa kuti akanenedwa, kuwukiridwa ndi kuchititsidwa manyazi. Nthawi zina amalandiridwa ndipo amasamalidwa ngati osafunikira kuposa nkhoa zinazo, chifukwa chakuti anasochera. Ngati okhulupirira akufuna kubwezeretsa amene wasokera munjira yake, mpingo uyenera kukhala okhulupirika ndi omvetsetsa. Pamene sitienera kulandira zikhalidwe zonama ndi zolembedwa zake. Tiyenera

Ndipo Pamene Adayipeza Lyo

tionetse chifundo ndi kumvomera abale athu amene akufuna kuti abwerere muchipembedzo. M’busayo potenga nkhosayo mwachimwemwe pa phewa lake ndi kuonetsa m’chitidwe wokoma mtima ndi wachikondi umene tiyenera kukumbukira pano. Iye adakhazikitsa kukhala chitsanzo kwa nkhosa zonse za m’kholalo. Mwanjira ngati yomweyi onani zomwe bambo adachita pakhani ya fanizo ya mwana olowerera. Iye ataononga cholowa chake chonse ndi kukhala moyo wochimwa, iye adabwerera kunyumba ya bambo ake.

Ndipo iye adanyamuka napita kwa abambo ake. Koma iye akanali patali, abambo ake anamuona ndipo anamvera chisoni; anamthamangira mwanayo, namukumbatira ndi kumupsopsona. Mwanayo anati, Abambo, Ine ndachimwira Kumwamba ndi inunso, Ine sindiyenera konse kutchedwa mwana wanu. Koma bamboyo anati kwa a ntchito ake, Fulumirani! Bweretsani mkanjo wabwino kwambiri ndipo mumuveke. Muvekeni mphete ndi nsapato. Bweretsani mwana wang’ombe wonenepa ndipo iphani. Tiyeni tikhale ndi phwando ndi kukondwera. Pakuti mwana wangayu adali wakufa, ndipo ali ndi moyoso; iye anatayika ndipo wapezeka. Chomwecho anayamba kukondwerera.” (Luka 15:20-24)

Mwanayo sadabwerere kwa bambo oti azikamunyoza ndi kumuweruza. Iye adabwerera kwa bambo wa chimwemwe amene adamulandira bwino. Ifenso tayenera tichite izi pamene nkhosa zotayika zikubwerera ku khola kwawo.

Nkhosa Yotayika

Valani Mavuto a Nkhosa Yotayika

Wonani pano kuti pamene m'busa adanyamula nkhusa ija, iye adanyamula kulemera konse kwa nkhusa ija pa phewa lake. Taganizani kuti mavuto onse a nkhusayo adali pa m'busa uja pamene amabwerera kukhola. Kumbuyo kwake kudali nkhusa yopanda ukhondo ndi yosweka mtima. Mwina iyo imatuluka magari ndipo magariwa amaononga mkanjo wa m'busayo. Kodi mudanyamulapo katundu wa munthu wosochera? Munthu wosochera nthawi zambiri amayenera kudziwa mmene angathetsere mkwiyo ndi kuwawidwa moyo kwake pa nkhusa yotayikayo. Nthawi zina kutayika kwake kumatha kubweretsa zovuta zina. Kunyamula nkhusayo pa phewa pake zikusonyeza kulolerana ndi kumvetsetsana atakumana ndi zovuta mmoyo wawo. Kulangizana kuti zinthu ziyambenso kuyenda bwino monga kale.

Kubwezeretsedwa ku Chiyanjano ndi Ntchito Zakale

Pamene m'busa uja adatenga nkhusa ija ndi kuyiyika pa phewa pake, iye adali ndi cholinga chimodzi mmaganizo mwake. Nkhosa iyi idzachira ndipo idzabwerera ku banja lake. Iyo idzakhalanso yofunikira ku ntchito ya mu ufumu wa Mulungu. Izi zidali choncho mmaganizo a m'busa uja.

Kalekale, ndidali ndi mwayi wokayankhula ku ndende mdziko la Philippines. Ndende iyi idali ya chitetezo chokhwima kwambiri chifukwa ndi kumene ankasungira mbamva zikuluzikulu za dzikolo. Mulungu wakhala akuchita zinthu zazikulu ku ndende kumeneko, ndipo a kayidi ambiri adamudziwa Yesu. Kunena moona, Mulungu wakhala akuyitana ena kumeneko kukhala a zibusu ndi kumatumikira akaidi azawo. Ine ndidapemphedwa kuti

Ndipo Pamene Adayipeza Lyo

ndikayankhule pa msonkhano wa azitumiki a Mulungu 150. Koma ambiri amene adabwera adali akayidi amene amatumikira akaidi anzawo kundende. Ine sindikanatha kuthandiza ndi ndalama, koma ndidabwitsidwa ndi chisomo chodabwitsa cha Mulungu, kuti atha kupulumutsa anthu awa, ndi kuwayitananso ku ntchito yake.

Ine apa ndidaganiza za Mtumwi Paulo, yemwe adaukira mpingo, koma Mulungu adamuyitana ku ntchito yake ndi kumusandutsa iye kukhala kazembe nambala 1. Ine ndidaganiza za Davide amene adali wa chigololo, wakupha ndi wachinyengo, koma iye adayitanidwa ndi Mulungu ndi kudzakhala mfumu yayikulu ya Israel. Ndidakumbukanso za Petulo yemwe adakana Yesu katatu, koma iye adayitanidwa ndi Mulungu kukalalika Uthenga waukulu woyambirira pa tsiku la Pentekosite umene udapangitsa anthu 3,000 kulandira Yesu.

Pali chiyembekezo pa nkhusa ina ili yonse. Mulungu sadzataya ndi kusiya nkhusa yotayika. Iye akufuna iyo itabwerera kukhola kwake ndi kuikidwa pamalo oti ipindule mu ufumu wake. M'busa uja adabwerera ndi nkhusa yotayika paphewa pake ndi cholinga chimodzi, choti ibwezeretsedwe ndi kupindulanso pa ntchito ya Mulungu. Nkhosa zonse ndi zofunikira. Ngakhale zimene zinatayika, iye sadzazisiya kunja. Cholinga cha Mulungu ndikubwezeretsa izo kukhola kwake. Tatiyeni tonse tichite motere ndi nkhusa zotayika masiku athu ano.

Zoyenera kuziganizira mwapadera:

- Kodi okhulupirira ena akuchita zotani kwa nkhusa yotayika?

Nkhosa Yotayika

- Kodi chimwemwe cha m'busa pamene adapeza nkhusa yake chikutiphunzitsa chiyani pa mmene m'busa amamvera pa nkhusa zake.
- Kodi zikusiyana chiyani potetezera ziphunzitso ndi potetezera mikhalidwe yamoyo ndi kukonda nkhusa? Kodi ndikotheka kutetezera zinazi koma osakonda nkhusa?
- Kodi kunyamula nkhusa paphewa zikutanthauzani? Chifukwa chiyani nkhusa yotayika iyenera kunyamulidwa kwa kanthawi?
- Kodi mungachite zinthu ziti kuti muthandize nkhusa yotayika kuti ibwerere kwa mbuye wake?
- Kodi mpingo wanu umasalira motani nkhusa zimene zikufuna kubwezeretsedwa ku mpingo wawo?

Zoyenera Pemphero:

- Pemphani Mulungu kuti akupatseni mtima ngati wa Yesu pa nkhusa zotayika.
- Pemphani Mulungu kuti akuthandizeni kuti muthandize nkhusa zotayika zomwe zabwerera kuchiyanjano
- Tengani kanthawi pang'ono ndikupempherera m'bale ndi mlango yemwe ali mnyengo zowawitsa. Pemphani Mulungu kuti azivumbulutse yekha kwa iwo, ndi kuwabwezeretsa kukhala chiwalo chifunikira cha thupi la Yesu Khrisitu.

Ndipo Pamene Adayipeza Lyo

- Pemphani Mulungu kuti akukhulukireni pa mawu oipa amene munanena amene alepheretsa wina kubwerera ku chiyanjano ndi Mulungu.

6 - Sangalalani Nane Pamodzi

Kenaka anayitana amzake ndi anansi pamodzi, ndi kuti, kondwerani nane, Ine ndayipeza nkhoa yanga yotayika ija. ' (Luka 15:6)

Kupeza nkhoa ndi gawo limodzi yandondomeko yakubwezeretsa. Chotchinga kwambiri pobwezeretsa nkhoa yotayika ndi nkhoa zina zimene zilli kale mkhola. Ine ndakumana ndi anthu ambiri amene akulephera kubwerera ku mipingo yawo chifukwa cholingalira ndi kuopa kuti kodi ndikalandidiridwa motani ndikabwerera. M'busa wanzeru wayenera kudziwa izi, ndikupeza njira zolandirira nkhoa zotayika zomwe zabwerera mkhola lake kuti zimzake ziyilandire bwino ndi kuyimvomereza.

Tangaonani zimene zimachitika nkhoa yotayika itabwerera. Vesi 6 limatiuza kuti iye anayitana azimzake ndi anansi pamodzi ndikuwapempha kuti akondwera naye limodzi chifukwa iye wapeza nkhoa yake yomwe inatayika. Vesi limeneri ndilofunukira zedi ngati ife tifuna timvetsetse chimene chikunenedwa poyankhula **zakubwezeretsa nkhoa yotayika mkhola mwake.**

Mfunso lomwe tiyenera kudzifunsa pano ndi ili: Kodi ndi chifukwa chiyani m'busa anayitana azimzake ndi anansi pamodzi? Tiyeni tingaona ena chabe mwa mayankho a funso limeneri.

“Kundwerani nane pamodzi”

Chifukwa chathu choyamba chikubwera chifukwa cha kapanda mneni uyu **“Kondwerani nane limodzi.”** M’busa atapeza nkhoa yake yotayika adali ndi chisangalalo chochuluka moti sakanatha kusangalala yekha popanda azimzake ndi anansi. Iye adayenera ndithu kugawana chisangalalochi ndi azinzake ndi anansi. Cholinga chake chidali choti asangalale kuti nkhoa yake yapezeka, ndipo iye anayitana azimzake ndi anansi kuti adzakondwere naye limodzi. Izi zikufotokozerana mmene m’busa ameneyu amayikondera nkhoa yake imene inatayika.

Kumbukirani kuti nkhoa imeneyi idamwazika kuchoka kukhola kwake. Mwina mwake idakodwa mutchimo kapena chiphunzitso chabodza. Mwina iyo idawononga khola pochoka. Nkhosayi mwina idali nthawi zambiri chizunzo ku mpingo. Kodi ndi kwabwino kungoyisiya nkhosayi kuti izipita ndi kuyiwala? Koma mtima wa m’busa udali wosweka chifukwa cha nkhoa yake imene inatayika. Iye adafunitsitsa itabwerera kukhola kwake. Iye wosangalala kwambiri chifukwa chakubwera kwa nkhosayi. Iyi sinthawinso yodzudzula ndi kuweruza. Moteromonso nkhoa zambiri zimabwerera ndi kudzalidira zilango ndi mpingo. Izo zimaweruzidwa, kudedwa, kudzudzulidwa mwankhaza ndi kuchitidwa miseche. Ichi sichikhalidwe cha m’busa uyu. Iye adayitana azimzake ndi anansi ake onse kuphwando lalikulu, kusangalalira kubwerera kwa nkhoa yake yotayika.

Pamene wobalalika wabwerera, iye amadzimva kukhala wamanyazi. Iye amadzimva kukhala wosayenerera pagulupo, ndipo nthawi zambiri amakhala chete pa maso pa ena amene akuoneka kukhala **“nkhoa zoyera kwambiri.”** Izi zikufananirapo ndi nkhani ya mwana wolowerera yomwe imapezeka pa Luka

Sangalalani Pamodzi Nane

15:21. Taonani mmene iye adachitire bambo wake wachikondiyo atamulandira.

*'Mwana anati kwa atate ake, Atate,ine
ndinachimwira kumwamba ndi inu nomwe,
chotero sindiyenera kutchulidwanso
mwana wanu.*

Ngakhale zinali choncho,koma atate a mwanayo anayitanitsa ng'ombe yamphongo yonenepa bwino, kuti iphedwe kuti akondwerere kubwerera kwa mwana wake. Kodi mukuganiza kuti izi zinamveka motani mumtima mwa mwana uja? Kodi izi sizidamutsimikizire za chikondi ndi chisangalalo cha atate ake chifukwa cha kubwera kwake? Phwando limeneri lidachitira umboni kwa mwanayo kuti atate ake akondwera ndi kubwera kwake. Machimo ndi upandu wake, kaye zidali zazikulu motani, koma sizidachotse chikondi cha atate ake pa iyeyo. Pamene m'busa anabwerako, ndi kuyitana anansi ake pamodzi, iye samangoonetsa chisangalalo kwa anansi ake, kapena nkhoa zina zija, koma kuti, nkhoa yobwererayo imve kulandiridwa ngati gawo limodzi la ziweto zake, ndipo kuti ipitirize pamene idasiyira.

Kodi ndi chophweka motani, kuti pamene tabalalika ndi kugwa m'machimo ndi upandu, koma ndi kumadziwa kuti Mulungu atha kutikondabe. Tipemphere kuti tichotse nkhoa zonse zimene timakhala nazo. Kumakhala chisangalalo Kumwamba pamene munthu mmodzi wotayika wabwerera kwa Mulungu. Mwina mwake anthu ena akuzungulirani atha kukudani, kukuweruzani kapena kunenani, koma Mulungu amakhala akusangalala. Iye amakondwera ndi kubwerera kwanu Kumwamba.Manja ake ali otsekuka zedi kuti akulandireni.Iye amalandira inu ndi chimwemwe. Izi zikutsimikizireni inu.Ichi chikhale chitsanzo kwa ife cha mmene tingalandilire nkhoa yotayika. Cholinga cha

Nkhosa Yotayika

Mulungu ndi kukhululuka ndi kuyiwala. Izi zaonekeratu pa chiphunzitso cha Masalimo 103:11-12

Pakuti monga Kumwamba kuli kutali ndi dziko lapansi, koteronso chikondi chake n'chachikulu kwa iwo amene amamuopa. Monga kummawa kutalikirana ndi kumadzulo, koteronso lye watichotsera mphulupulu zathu kuti zikhale kutali nafe.

“Ine ndapenza nkhusa yanga yotayika”

Palonso chifukwa china chimene m’busa adayitanira azimzake ndi anasi kuti adzakondwere naye limodzi chifukwa chakupezeka kwa nkhusa yake yomwe idasowa. Ichi chitha kupezeka mumkapanda mneni uyu ***“Ine ndapenza nkhusa yanga yotayika.”*** M’busayu akufotokoza zinthu ziwiri momveka bwino pamenepa. Choyamba, nkhusa yotayika yapezeka, ndipo chachiwiri, nkhusayo idali yake.

Kulengeza poyera ndikofunika kwambiri pa zifukwa ziwiri. Choyamba, kumabweretsa nkhusa yotayika pafupi. Ichi chili ngati fundo yokhululukira, kulandira ndi kutsimikizira. Chonde tisaphweketse ubwino wa kungeza pagulu pa moyo wa membala ku mpingo. Ine ndikukumbukira nthawi ina yake pamene ndidali kulalika pa mpingo pena, munthu wina mumpingomo, sadasangalale ndi chimene ine ndidanena. Iye adatuluka mumpingomo pomenyetsa chitseko, ndi kunena motsimikizira kuti achita chithekera china chilichonse kuti ine ndisadzalalikaponso pa mpingopo. Pamene atsogoleri a pampingopo adamva ichi, iwo adakhilirana pansi. Zotsatira zake zidali kalata yawo kwa ine yotsimikizira kuti akusangalala ndi utumiki wanga ndi mawu amene ndidanena aja. Kalata imeneyi idabweretsa chilimbikitso

Sangalalani Pamodzi Nane

kwa ine ndi kunditsimikira za ubale wathu ndi mpingowo. Pamene tilibe chitsimikiziro cha ubale wathu ndi mpingo, timakhala opanda ufulu wotumikira ndi kuchita chiyanjano monga momwe kuyenerera kukhalira. M’busa wanzeru wayenera kudziwa kuti pamene nkhusa yotayika yabwerera kukhola kwake, yayenera kumva kulandiridwa ndi mpingo wonse.

Pali chifukwa chachiwiri chimene nkhusa yotayika yayenera kulandiridwa ndi mpingo wonse. Ichi ndi chinthu chabwino kwa nkhusayo ndi nkhusa zomwe zidali kale mkholamo. Mpingo wayenera kudziwa kuti nkhusa yotayika yalandiridwa. Kubwezeretsedwa kulibe phindu, ngati mpingo ukudziwa kuti padakali zinthu zina zoyenera kukonzedwa. Pamene mukulengeza poyera kuti nkhusa yotayika koma tsopano **“Yapezeka”**, m’busa akuthetsa zokamba kamba ndi miseche zimene zingabwere zokhudza nkhusayi. Iye akulengeza kuti nkhusa yatha, ndipo tatseka buku yankhaniyo. Ichi chimatsegule makomo a maubwenzi atsopano ndi nkhusayi

Kuyang’ana nkhusa yotayika kumamulowetsera zambiri m’busa, komanso kuyibweretsa kunyumba sinkhani yophwekaso. Mipingo nthawi zambiri simavomereza kulandira nkhusa yotayika. M’busa amayenera kuti apoletse mabala amene nkhusa yotayikayo idabweretsa kwa nkhusa zomwe ziri kale mkholamo. Kukhululukidwa zikukhala kophweka nthawi zonse. Kudalirana ndi kukhulupirirana kwayenera kubwezeretsedwanso. Kulengeza pagulu mumpingo kuti nkhusa ija yapezeka sizimangofuna mawu okha basi. M’busa wanzeru amayenera kukonza pa malo kuti ena akhululuke ndi kuyilandira nkhusa yotayiko yomwe tsopano yabwerera. Izi zimayenera m’busa akambirane ndi nkhusa zina zimene siziri zokonzeka kukhululuka. Iye wayenera kuti wathetsa mayankhulidwe woononga, zochita zonyasa zomwe zingabwereretse nkhusa ija kupanga nawo chiyanjano pampingo.

Nkhosa Yotayika

Kubwezeretsa nkhoa yotayika, ndi kutanthauza kukonzekeretsa mpingo kuti uyilandire. M'busa wanzeru amachita mwa nzeru kuti nkhoayi ilandiridwe mumpingo.

Zoyenera kuganiza mwapadera :

- Tafananitsani chikhalidwe cha m'busa uyu ndi chikhalidwe cha mpingo wanu kwa nkhoa zotayika zomwe za bwerera. Kodi mpingo wanu uli ndi chikhalidwe ngati cha m'busa uyu?
- Chifukwa chiyani chili chofunikira kwambiri kwa nkhoa yotayika kutsimikiziridwa ndi chikondi ndi chisamaliro chathu? Kodi mukuona kufanana kotani pakati pa kulandiridwa ndi kusunga mwambo?
- Kodi m'busa ali ndi udindo wotani pokozekeretsa mpingo polandira nkhoa zotayika? Kodi m'busa ayenera kukoza zotchinga ziti pamene akukonzekeretsa mpingo polandira nkhoa zotayika?

Zoyenera Pemphero :

- Tiyeni tipemphere kwa Mulungu kuti achotse mtima woweruza ndi kudzudzula pamene tikulandira nkhoa zotayika zomwe zabwerera mumpingo.
- Tiyeni tipemphe Mulungu kuti atithandize kuti tikhale wokoma mtima ndi a chikondi kwa abale wotayika ndi wobalalika mu Uzimu.

Sangalalani Pamodzi Nane

- Tiyezi titenge kamphindi pang'ono ndi kupempha Mulungu kuti athandize mpingo wathu kuti ukhale wodziwa kulandira nkhoa zotayika.
- Tiyezi tipemphe Mulungu mmene tingalandirire nkhoa zotayika pa ife tokha ngati wokhulupirira.

7 - Kusangalala Kumwamba

*Ine ndikukuuzani kuti momwemonso
kudzakhala chikondwerero chachikulu
Kumwamba chifukwa cha ochimwa
mmodzi amene watembenuka mtima
kusiyana ndi anthu olungama 99 amene ali
otembenuka mtima kale(Luka 15:7)*

Yesu adamaliza fanizoli pa vesi 7 ponena kuti Kumwamba kumasangalala kwambiri munthu mmodzi ochimwa akatembenuka mtima koposa anthu 99 Oyera kale mtima amene safunika kulapanso.Kuti tidziwe chimene Ambuye akunena pano, ife tayenera poyamba tidziwe kuti kodi Mulungu amamva bwanji pa nkhani za anthu ake.Chonde dekhani kaye ndikulingalira zimene mneneri Zefaniya pa Zefaniya 3:17 adanena zokhudza ubale wa Mulungu ndi anthu ake:

*.Ambuye Mulungu wanu alinanu, ndipo ndi
wamphamvu pokupulumutsani. Iye amasangalala
nanu. Iye adzakhalitsani chete ndi chikondi chake.
Iye adzakondwera nanu mkuyimba.*

Mulungu wayankhula zambiri pa vesi limeneri zokhudza ubale wake ndi anthu ake.Wonani pano kuti Iye ndi Mpulumutsi wawo. Iye amafikira kwa iwo pamene akumufuna ndipo amawapulumutsa. Wonaninso kuti Iye amasangalala ndi anthu ake, amawakonda ndi kukondwera nawo podzera mkuyimba. Anthu a Mulungu amabweretsa chikondwerero ku mtima wa

Nkhosa Yotayika

Mulungu. Ngakhale iwo ali osalungama kweni-kweni, komabe amadzaza mtima wa Mulungu ndi kuyimba.

M'bukula Yesaya, Mulungu anafanizira ubale wake ndi ana ake monga momwe ubale umakhalira pakati pa mayi ndi mwana wake. Timawerenga izi pa Yesaya 49:15-16:

Kodi mayi atha kuyiwala mwana wake kubere kwake ndi kukhala wopanda chifundo kwa mwana amene wam'berekayo? Ngakhale iye atayiwala, koma Ine sindingayiwale inu!! Taonani ndafukwata inu m'manja mwanga mwa chikondi; ndipo moyo wanu onse uli pa maso panga.

Ndi chinthu chophweka mayi kuwayiwala mwana wake amene akuyamwa, kusiyana ndi Mulungu kuyiwala inu. Izi zili choncho chifukwa Mulungu ndi wokoma mtima ndi wachikondi. Kodi ndi ndani mwa ife amene sadziwa za chisangalalo chimwene mwana wongabadwa kumene amabweretsa kwa mayi ake? Dziwani pano kuti Mulungu wafukwata ana ake mmanja mwake. Mwanjira ina, mayina awo ali pa maso pake. Ndipo lye sadzawayiwala.

Mulungu akufaniziranso ubale wake ndi anthu ake monga momwe ubale umakhalira pakati pa mkwati ndi mkwatibwi. Izi zalembedwa pa Yesaya 62:5 pamene Mulungu akunena kuti:

Monga mnyamata amakwatira namwali, ndipo Mkwati amakondwera ndi mkwatibwi, chonchonso Mulungu adzakondwera nawe.

Apanso nkhani ndi ya kukoma mtima, chikondi ndi chikondwerero.

Kusangalala Kumwamba

Chikondi chachikulu cha Mulungu pa anthu ake sichidzasintha. Ichi ndi chikondi chosatha chimene mneneri Yeremiya ananena pa Yeremiya 31:3:

'Ine ndinawaonekera ndili chapatali ndipo ndinati, Ine ndakukonda ndi chikondi chopanda malire. N'chifukwa chake ndipitiriza kukukondani.

Chikondi cha Mulungu kwa anthu ake sichimatengera kuti ndinu abwino kwambiri, kapena kuti mumakhala moyo wokondweretsa Mulungu. Iye amatikonda nthawi zonse mosatengera nyengo zimene tili. Mtumwi Paulo pa Aroma 5:7-8 pamene ananena kuti, pamene tili nyengo zowawitsa Yesu anaonetsa chikondi chake chachikulu kwa ife.

Mzotheka kawirikawiri munthu wabwino kufa chifukwa cha munthu oipa, pamene munthu amatha kufa mophweka chifukwa cha munthu wabwino. Koma Mulungu adaonetsa chikondi chake pa ife, kuti ngakhale tili wochimwa Yesu adatifera ife.

Yesu Mwini wake ananena kuti “Palibe chikondi china choposa ichi, kuti wina akapereke moyo wake chifukwa cha abale ake” (Yohane 15:13). Yesu adachita zina zikuluzikulu kuposa apa. Komabe Iye adapereka moyo wake chifukwa cha ife ngakhale tili adani ake.

Kuyankhula ndi ophunzira ake pa Yohane 14:1-3, Yesu ananena kuti:

Mtima wanu usavutike. Khulupirirani Mulungu; khulupirirani Inenso. M'nyumba mwa Atate anga muli zipinda zambiri. Kukanakhala kuti mulibemo ndikanakuwuzani. Ine ndikupita kumeneko

Nkhosa Yotayika

*kukakukozerani malo,ndipo ndikapita
kukakukozerani malo, ndidzabweranso,
kuti kumene kuli Ineko inunso mukakhale
komweko.*

Ndicholinga cha Ambuye Yesu kuti tidzakhale ndi Iye kwa muyaya. Pali anthu amene titha kukhala nawo kwakanthawi, koma pali anthu ochepa okha amene amafuna atakhale nawe kwa muyaya. Chikondi ndi chifuniro cha Yesu ndi chokuti tikakhale pa maso pake kwa muyaya. Iye sadzatopa nafe. Chikondi chake ndi chimwemwe chake mwa ife sichidzatha.

Kodi izi zikutiuza chiyani za chikondi cha Mulungu pa anthu ake? Iye amasangalala mwa iwo ndipo amawakonda ndi chikondi chachikulu choposa chimene mayi amakhala nacho pa mwana wake. Iye adalolera kutaya moyo wake kuti aonetse kuzama kwa chikondi chake pa anthu ake. Cholinga chake ndi chikuti ife tidzakhale pa chikondi ndi chiyanjano ndi Iye kosatha. Padalibenso chikondi china choposa ichi.

Chikondi cha Mulungu pa anthu ake ndi chikondi cha mphamvu ndi chachikulu. Kodi Yesu akutiuzza chiyani pa Luke 15:7? Komabe, kumakhala chisangalalo Kumwamba pamene mmodzi ochimwa watembenuka mtima koposa anthu 99 amene anatembenuka kale mtima. Tatiyeni titaganizira bwino pa fundo imeneyi kwa kanthawi. Mwina mutha kutenga chikondi ndi chisangalalo ichi ndikuchiyika malo ena ake. Nanga kodi titachita mofanana ndi wotembenuka mtima onse 99 amene akunenedwa mfanzoli. Kodi chimulu chachisangalalo chake chitha kukhala lotani? Tatiyeni titenge chiphiri cha chisangalalo ndi kuchipereka kwa nkhoa yotayika. Ichi ndi chimene Yesu akunena pamenepa. Izi sizikutanthauza kuti Mulungu amakonda pang'ono anthu abwino ai. Izi zikutionetsa

Kusangalala Kumwamba

mmene Mulungu amamvera ndi nkhoa yotayika ndi yomwazika. Kodi izi zikutanthauza chiyani kwa ife lero lino?

Ngati tikufuna kusangalatsa mtima wa Mulungu, palibe chomwe mungachite choposa kufunafuna nkhoa zotayika ndi kuzibwezeretsa kwa Mulungu. Nthawi yathu yambiri yatayika potumikira nkhoa 99 zomwe sizikufunika kulapa. Mtima wa Mulungu uli poti izi 99 zikule ndi kukhwima pa Uzimu, koma mtima wa Mulungu umasweka ndi nkhoa zosokera zimene zataya njira zawo. Ngati tifuna timusangalatse Mulungu, tayenera kuti titsekule maso athu ndi kuoona zosowekera za nkhoa zotayika zomwe zatizungulira. Mulungu akumva kulira kwa izo kuti zikufuna thandizo lathu. Mtima wa Mulungu umasweka poona nkhoa zotayika zikusiyidwa ndi kuyiwalidwa kuseri kwa phiri zikuonongeka. Mtimu wa Mulungu umasweka kwambiri akamaona mmene azibusa alero agonthetsera makutu awo osamamva kulira kwa nkhoa zotayika.

Tamvani zimene Yesu akutiiza pa Mateyu 25:40:

*Zoonadi, ndikukuuzani kuti chilichonse
chimene munachitira mmodzi mwa abale
anga onyozekewa munandichitira Ine.*

Ubale wa Yesu ndi ana ake, ndiwakuya, kotero kuti choipa chimene tichitira imodzi mwa nkhoa zake zotayika tikuchitira Iyenso. Amamva mmene izo zimamvera. Machenjezo ambiri m'Baibulo akunena zoipa zomwe timapanga pa abale ake a Yesu. Taganizirani zimwe Eksodo 22:22-24 akunena:

*Musadyere masuku pa mutu a zimayi
amasiye, kapena ana amasiye. Ngati
muchita ichi, ndipo kulira kwawo kufika kwa
Ine, pompo Ine ndidzamva kulira kwawo.
Mkwiyo wanga udzakula, ndipo ndidzapha*

Nkhosa Yotayika

*ine ndi mpeni, azikazi anu adzakhala
amasiye ndipo ana anu adzakhala opanda
bambo.*

Chilango chodyera masuku pa mutu azimayi ndi ana amasiye
chidali imfa yobaidwa ndi mpeni. Mulungu adzamva kulira kwa ana
ake ndipo adzaonetsa chilungamo chake.

Mchipangano chatsopano mulinso machenjezo ngati awa.
Mvetserani zimene Ambuye wathu Yesu akunena pa Maliko 9:42:

*“Ndipo ngati wina aliyense achimwitsa
mmodzi wa ana ang’ono awa amene
akhulupirira Ine, Kukanakhala bwino kwa
iye kuti aponyedwe m’nyanja
atamangirirdwa mwala waukulu m’khosi
mwake”*

Kuyankhula kwa azibusa a nthawi ya Ezekiel amene ankadyera
masuku pa mutu nkhusa za Mulungu, Mulungu adanena kuti pa
Ezekiel 34:7-10

*’Chconcho inu abusa, tamvani zimene Ine
Yehova ndikukuwuzani. Pali Ine wamoyo,
akutero Ambuye Wamphamvu zonse,
ndithu, nkhusa znaga zinajiwa ndi zirombo
zakuthengo, zinasanduka chakudya cha
zirombo chifukwa panalibe abusa. Abusa
anga sanafunefune nkhusa zanga. Iwo
ankangosamala za iwo okha m’malo
mosamala nkhusa zanga. Chifukwa chake,
inu abusa tamvani zimene Ine Yehova
ndikukuuzani. Ine Ambuye Yehova ndikuti
:Ine ndayipidwa nanu, inu abusa.
Ndidzakulandani nkhusa zanga ndipo
simudzazidyetsanso. Ndidzakuchotsani pa
ntchito ya ubusa kuti musamangodzidyetsa*

*Kusangalala Kumwamba
nokha.Ndidzalanditsa nkhoa zanga
kukwamwa kwanu ndipo simudzazidyanso.*

Mulungu waima njii kutetezera nkhoa zake zotayika. Iye amathana ndi amene akuzuza nkhoa zake zotayika posamva kulira kwa izo. Kodi inu mutha kusangalatsa mtima wa Mulungu kudzera mkusamalira nkhoa zake zotayika? Kodi muyamba kugawo chikondi ndi chifundo cha Mulungu kwa nkhoa zake zotayika?.

Ngati muli mmodzi mwa nkhoa zotayikazi, dziwani lero kuti Yesu akudziwa zosowa zanu.Iye akuona kubalalika kwanu. Mutha kukhala osakonzeka kubwerera kwa Iye, koma Iye sadzakutayani. Iye amafuna mukhale naye pa chiyanjano.Iye akudikira inu. Iye sadzalola inu mutayike. Tamverani zimene Mulungu akunena pa Hoseya 2:5-7:

*"Amayi awo akhala akuchita za
chiwerewere, ndipo anawabereka anawo
akuchita zinthu zochititsa manyazi. Iwo
anati, Ine ndidzatsatira zibwenzi zanga,
zimene zimandipatsa chakudya ndi madzi,
ubweya ndi thonje, mafuta ndi chakumwa.
Choncho njira yake ndidzayitseka ndi
minga, ndidzamuzinga ndi khoma kotero
kuti sadzapezanso njira yotulukira.
Adzathamangira zibwenzi zake koma
sadzazipeza;adzazifunafuna koma
sadzazipenza. Pamenepo iye adzati,
Ndubwerera kwa mwamuna wanga
woyamba uja, pakuti ndinali pabwino ndi
iyeyo kusiyanyitsa ndi pano.*

Israel ankafuna mabwenzi ena koma Mulungu sadamusiye kuti apite. Pa Hoseya 4:6 Mulungu akuti "Choncho njira yake ndidzayitseka ndi minga, ndidzamuzinga ndi khoma kotero kuti

Nkhosa Yotayika

sadzapezanso njira yotulukira. Mulungu sadzawaleka anthu ake kuti awonongeke ngakhale ali a upandu ndi umbanda. Mulungu amasaka ana ake mpaka atawapeza.

Ngati muli nkhusa yotayika lero lino, zindikirani kuti Mulungu amakukondani. Iye adzakufunafunani inu ndipo sadzalola wina kumulanda inu. Mutha kumathawa Mulungu ndi mphamvu zanu zonse, koma tsekulani maso anu ndipo mudzaona kuti alibe kumabli yanu. Dziperekeni ku chikondi cha Mulungu. Tsegulani mtima wanu kwa Mulungu, ndipo Iye adzakusamalirani nthawi zonse.

Pemphero langa pa phunziro lino lili magawo awiri. Choyamba kuonetsa anthu chimene chili mumtima wa Mulungu kwa ana ake amene asochera njira zawo. Ngati muli nkhusa yotayika, chonde sangalalani ndi ichi. Ngati muli mmodzi mwa nkhusa 99, chonde dziwani kuti Mulungu amakondanso kwambiri nkhusa imodzi imene yatayika.

Chachiwiri, ndikukhulupirira kuti phunziro lino litsegula maso kuti muone nkhusa zotayika zimene zakuzungulirani, zimene zikulira kufuna chithandizo ndi chisamaliro. Mulungu asangalatsidwa ndi phunziro lino, kuti likapange wowerenga kuti akathe kuona kufunika kwa utumiki wotumikira nkhusa zotayika. Mulungu adzakondwera kwambiri akadzaona anthu amabiri amene awerenga buku lino akukatumikira mwa chikondi ndi chifundo kwa nkhusa zovulazidwa, zosiyidwa ndi zobalalika.

Kusangalala Kumwamba

Zofunika kuziganizira mwapadera:

- Kodi Baibulo likuti chiyani za mmene amamvera zokhudza ana ake?
- Kodi Mulungu amamva bwanji zokhudza nkhusa zotayika? Kodi machimo ndi upandu wathu amathetsa chikondi cha Mulungu pa ife?
- Kodi nkhusa zotayika ndi ndani mdera lathu? Kodi ndi chiyani chiti chimene chingachitike kuti tikatumikre izo?
- Taona pa Mateyu 25:40 kuti Yesu adadzidziwitsa kwa nkhusa zotayika. Kodi izi zikutiphunzitsa chiyani ife amene tikufuna tikabweze nkhusa zotayika ndi zobalalika pafukwa zosiyanasiyana

Zofunika Pemphero:

- Mfuseneni chikhululukiro Mulungu chifukwa chosowa chikondi kwanu pa anthu otayika.
- Penzani nthawi ndikupemphera munthu wina amene wasweka mtima ndipo akufuna m'busa kuti akamusamalire.
- Mfuseneni Mulungu kuti akupatseni chifundo chachikulu pa nkhusa zotayika. Mpempheni Mulungu kuti atsegule maso anu kuti muone nkhusa zotayika, ndinso makutu anu kuti mumve kulira kwa nkhusa zotayika.
- Thokozani Mulungu amene amatikondabe ngakhale tili anthu ochimwa.

Light To My Path Book Distribution

Bungwe la Light To My Path Book Distribution(LTMP) limalemba ndi kugawa mabuku kuti afikire anthu osowa amene akugwira ntchito ya Mulungu ku Asia, Latin America ndi Africa. Anthu ogwira ntchito ya Mulungu m'mayiko amene akutukuka kumene alibe kuthekera kotha kupeza maphunziro abwino a Baibulo, kapena kugula kumene zipangize za mautumiki awo ngakhaleso za iwo eni. M'bale F.Wayne Mac Leod ndi membala wa bungwe la Action International Ministries, ndipo iye wakhala akulemba mabuku awa ndi cholinga chowagawa aulere kapena kugulitsa pamtengo wosaboola mthumba kwa azibusa ndi anthu ena omwe, amene akugwira ntchito ya Mulungu pa dziko lonse lapansi.

Lero lino, mabuku ake zikwi zikwi akugwiritsidwa ntchito polalika, pophunzitsa, posodza anthu ndi kulimbikitsa anthu pa moyo wa Uzimu m'mayiko oposa 60. Mabukuwa lero atanthauziridwa mziyankhulo zambiri m'mayiko osiyanasiyana. Cholinga chake ndichoti mabukuwa afikire anthu ambiri pa dziko lonse lapansi pano ngati kutakhala kutheka.

Utumiki wa LTMP umadalira chikhulupiriro ndi kudikira kwa Mulungu kuti upeze zipangizo zogawira mabukuwa kuti akalimbikitse and kulangiza anthu okhulupirira pa dziko lonse lapansi pano. Kodi mungapemphere kwa Mulungu kuti atsegule makomo kuti mabukuwa atanthauziridwe mziyankhulo zambiri ndi kugawidwa mwakathithi m'madera ambiri pa dziko lapansi lino.?

Kuti mudziwe zambiri za utumiki wa Light To My Path(LTMP) chonde onani pa tsamba la makina a intaneti la ["https://www.lighttomypath.ca/"](https://www.lighttomypath.ca/)